



تلاوت کی فضیلت

UBWINO
**WOWERENGA
QURAN YOYERA**



Mteopoleli wa Ahl-e-Sunnat
Majumabizi wa Dawat-e-Islami, Alimul Madani Abu Bilal
MUHAMMAD ILYAS
Attar Qadiri Razavi

مفت محمد عیسیٰ
رحمۃ اللہ علیہ



الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

Du'ā yowerengera Buku

Werengani Du'ā (pemphero) musanayambe komanso mukamaliza buku kapena phunziro lililonse la Chisilamu, muzakumbukira chilichonse chomwe mwawerenga,

إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَاَنْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَامِ

Kumasulira

Yā Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a Chidziwitso komanso a luntha ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli Wolemekezeka kwambiri komanso Wawulemerero!

(Al-Mustatraf, vol. 1, pp. 40)

Dziwani: Nfunireni zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ) kamodzi musanayambe komanso mukamaliza Du'ā.

تلاوت کی فضیلت

Tilāwat kī Fazīlat

Ubwino owerenga buku

LOLEMEKEZEKA LA QURAN

Kabukuka kanalembedwa ndi Shaykh-e-Tarīqat Amīr-e-Ahl-e-Sunnat, muyambisi wa Dawat-e-Islami ‘Allāmah Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دامت برکاتہم العالیہ mu chilankhulo cha Urdu. **Nthambi Yomasulira** yamasulira mu Chichewa. Ngati mungapeze kulakwika kulikonse mu kamasuliridwe kapena mukalembedwe, chonde ziwitsani Nthambi Yomasulira pa makeyala kapena imelo ali m’mutsiwa ndi cholinga chofuna kupeza mphoto [Šawāb].

Nthambi yomasulira (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

Email: ✉ translation@dawateislami.net

Ubwino owerenga buku Lolemekezeka la Quran
Kumasulira mu Chichewa kwa ‘Tilāwat kī Fazīlat’



MA UMWINI ONSE NDI OTETEZEKA

Umwini © 2025 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukuli likuloledwa kusindikizidwanso, kapena kusinthidwa, mukawonekedwe komanso munjira iliyonse ngati, ya magetsi, zipangizo zilionse, kupanga kope kumene, kusungidwa kapena njira zina, popanda chilorezo cholembidwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

Kutsindikiza kwa chitatu: Jumadal Awwal, 1447 AH – (February, 2017)

Lamasuliridwa ndi: Majlis-e-Tarajim (Dawat-e-Islami)

Wosindikiza: Maktaba-tul-Madinah

Kuchuluka kwake: 3000

KUTHANDIZA

Khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandizira kusindikiza kwa buku lachipembedzo kapena kabuku kuti likhale Isal-e-Sawab kwa achibale anu omwe anamwalira.

Maktaba-tul-Madinah

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✉ **Email:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net

☎ **Phone:** +92-21-34921389-93

ZANKATIMU



Ubwino owerenga buku.....	1
LOLEMEKEZEKA LA QURAN	1
Kupambana konfunira zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ)	1
Kupambana kwa yemwe amayikonda Quran.....	2
Kupambana khumi kwa chilembo chilichonse.....	3
Munthu wabwino kwambiri.....	4
Quran idzawapemphera anthu chikhululuko ndikuwalowetsa ku Ntendere.....	5
Kupambana kophunzitsa vesi imodzi kapena Sunnah.....	6
Mphoto yabwino mpakana Tsiku Lachiweruzo kwa yemwe waphunzitsa vesi imodzi!.....	6
Allah amawonjezera mphoto zochuluka kufikira Tsiku Lachiweruzo.....	7
Analoweza magawo 15 a Quran adakali mu mimba molemekezeka mwa mayi ake.....	8
Ngale 21 za Madanī zokhuza kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran.....	10
Mwana wa Madanī anawulura chinsinsi!.....	17
Ndi Farḍi kwa Msilamu aliyense kuwerenga Quran Yolemekezeka molondora komanso kupewa kuwerenga molakwika	20
Kupambana kwa mwana wa Madanī yemwe akuwerenga Quran.....	21

Ngale 14 za Madanī zokhu Sajdaḥ Tilāwat.....	22
Pofuna kukwaniritsa zokhumba.....	26
Mavesi 14 a Sajdaḥ.....	27
Ngale 9 za Madanī zokhuza kugwira buku Lolemekezeka la Quran.....	29
Pempho la Madanī kwa otsindikidza.....	32
Ngale 4 za Madanī zokhuza kumasulira Quran Yolemekezeka ..	35
Ngale ziwiri za Madanī zokhuza kakwiriridwe/kamizidwe ka matsamba othothoka a mu Quran Yolemekezeka	37
Ngale 8 Zosiyanasiyana za Madanī.....	39
Ngale 5 za Madanī zokhuza kupanga Īṣāl-e-Šawāb	42
Ndondomeko ya kapangidwe ka Īṣāl-e-Šawāb.....	44
Ndondomeko ya Fātiḥaḥ.....	44
Ndondomeko ya kapangidwe ka Du’ā [pempho] la Īṣāl-e-Šawāb	49
Ngale 17 za Madanī zokhuza kumanga ‘Imāmaḥ [Sunnaḥ yomangira nduwira]	51
Poyambirira tinve kaye, ma Ḥadiṣ 6 olemekezeka Mustafa ﷺ	51



الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

Ubwino owerenga buku LOLEMEKEZEKA LA QURAN

Ngakhale satana atakuchititsani ulesi motani kuti muwerenge kabukuka, yesetsani kukamaliza konse; *إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ* mudzapedza uthenga wofunikira komanso maphunziro ochuluka.

Kupambana konfunira zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī ﷺ)

Mtumiki wathu Wokondedwa, yemwe ndi ntendere wa mu ntima komanso nzeru zathu, mwini kupereka kwambiri ndikuleza *صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ* walankhula kuti, ‘kundifunira zabwino pa ine ndi Nūr [kuwala] pa mulatho wa Ṣirāt. Aliyense yemwe angandufunoire ine zabwino kokwana ka 80 pa tsiku Lachisanu; Machimo ake a zaka 80 azakhululukidwa.’ (*Al-Mu‘jam-uṣ-Ṣaghīr*, pp. 320, Ḥadīṣ 5191)

Yehī hay ārzū ta ‘līm-e-Quran ām hō jāye

Ĥar aik parcham say aūnchā parcham-e-Islam hō jāye

Ndikupempha kuti ziphunzitso za Quran zipitirire; limeneri ndilo pemphero langa

Ndikupempha kuti mbendela ya Chisilamu ikhale pamwamba, kuposa mbendela zonse

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kupambana kwa yemwe amayikonda Quran

Sayyidunā Shaykh Šābit Bunānī قُدَّسَ سِرُّهُ التَّوَرَانِي kuwerenga anali kumaliza kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran kamodzi pa tsiku. Iye رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ anali kusala kudya usana komanso kupemphera Šalāh zowonjezera usiku. Anali kupemphera 2 Rak'āt ya Nafl Šalāh mu Masjid (nzikiti) uliwonse angaduse (ntundu wa Šalāh imeneyi imatchedwa kuti Taḥiyya-tul-Masjid). Mukufotokozera kwake pa mitendere imene anadalitsika nayo, iye anati, 'Ndamaliza kuwerenga buku lonse Lolemekezeka la Quran komanso kulira pa maso pa Rab عَزَّوَجَلَّ ndi chifupi komanso pa nsanamira iliyonse ya Jāmi' Masjid.'

Iye رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ anali kuyikonda kwambiri Šalāh ndi kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran, ngakhalenso ntundu uliwonse wa ntendere umene wadalitsika nawo. Zotsatila zake, pambuyo pakuchoka mu umoyo uno, nthawi yomukwilira mosayembekezeka chiduswa cha njelwa chinagwera mu zenje lake la manda. Ndipo pamene anthu akafuna kulowa kuti akatole chiduswa cha njelwa chija anali wodabwa kuwapeza komanso kuwawona Sheikh رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ anali chiyimire m'manda mwawo ndipo anali kupemphera Šalāh! Pamene akubanja anafunsidwa za ichi, mwana wake wokondeka wa nkazi anati: Olemekezeka bambo anga رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ anali kupanga dua iyi tsiku lililonse, 'E Allah عَزَّوَجَلَّ! Ngati mungapereke mwayi kwa munthu wina aliyense mwayi wopemphera Šalāh m'manda pambuyo pa infa

yake, ndiye muzandipase nane mwayi woterewu [muzandidalitse nawo].’

Zimanenedwa nthawi zonse kuti anthu amati akamadutsa pafupi ndi manda a Shaykh رحمته الله عليه, anali kumva kuwengedwa kwa buku Lolemekezeka la Quran kuchokera mu mkati mwa manda ake odalitsika. (*Hilya-tul-Awliyā*, vol. 2, pp. 362-366)

Timupemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti awachitire iwo chisoni komanso natikhululukira ife chifukwa cha chisoni chake!

أَمِينَ بِجَاهِ النَّبِيِّ الْأَمِينِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Kupambana khumi kwa chilembo chilichonse

Quran Yolemekezeka ndi Yawulemelero ndi mawu Opatulika a Allah عَزَّوَجَلَّ; kuwerenga Quran Yolemekezeka, kuphunzitsa Quran Yolemekezeka, kunvera Quran Yolemekezeka, komanso kuwerenga Quran ndi kuti ena amvetsera kuwerengedwako, zonsezi ndi ntchito zamalipiro ochulukwa. Kuwerenga chilembo chilichonse cha buku Lolemekezeka la Quran, munthu amapeza zabwino khumi. Mukulemekezeka kotere, Mtumiki Wodalitsidwa komanso Wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti, ‘Yense angawelenge chilembo kuchokera mu buku Lolemekezeka la Allah عَزَّوَجَلَّ, azapeza mphoto yabwino imodzi yomwe ikufanana ndi mphoto zabwino khumi. Sindikutanthauza kuti الْم (Alif-Lām-Mīm) ndi

liwu limodzi ayi; koma kuti **أَلِف** (Alif) ndi chilembo chimodzi, **لَام** (Lām) ndi chilembo chimodzi, komanso **مِيم** (Mīm) ndi chilembo chimodzi.’ (*Sunan-ut-Tirmiẓī, vol. 4, pp. 417, Ḥadīṣ 2919*)

Tilāwat kī tawfīq day day Yā Ilāhī

Gunāḥaun kī ḥo dūr dil say siyāhī

*E Allah wanga! Ndipaseni kuthekera, kowerenga buku
Lolemekezeka la Quran
Ndi cholinga choti ntima wanga utsukidwe kuchokera ku
kusachita chilungamo*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Munthu wabwino kwambiri

Yemwe ali Mwini Nūr, Mtumiki Wolemekezeka **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** walankhula kuti: **خَيْرُكُمْ مَنْ تَعَلَّمَ الْقُرْآنَ وَعَلَّمَهُ** Kumasulira: Munthu wabwino kwambiri mwa inu ndi yemwe waphunzira buku Lolemekezeka la Quran, naliphunzitsa kwa ena. (*Ṣaḥīḥ Bukhārī, vol. 3, pp. 410, Ḥadīṣ 5027*)

Sayyidunā Abū ‘Abdur Raḥmān Sulamī **رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ** anali kuphunzitsa buku Lolemekezeka la Quran mu Masjid ndipo analankhula kuti, ‘Ḥadīṣ iyi yandipangitsa kukhazikika ine munomo.’ (*Fayḍ-ul-Qadīr, vol. 3, pp. 618, Ḥadīṣ 3983*)

Allah mujhay Ḥāfiẓ-e-Quran banā day

Quran kay aḥkāṁ pay bhī mujh ko chalā day

*E Allah! Ndipangeni ine kukhala Ḥāfiẓ wa Quran Yolemekezeka
Ndipo ndipangeni kukhala wokhazikika mu kutsatira malamuro
ake a Quran Yolemekezeka*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Quran idzawapemphera anthu chikhululuko ndikuwalowetsa ku Ntendere

Zafotokozedwa ndi Sayyidunā Anas رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ Mtumiki Wolemekezeka wa anthu, yemwenso ndi Ntendere wa mu ntima wathu komanso nzeru, wopereka komanso woleza صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti, ‘Yense yemwe waphunzira ndi kuphunzitsa buku Lolemekezeka la Quran, ndikugwiritsa ntchito chilichonse chomwe chili mu buku Lolemekezeka la Quraniyi; Quran idzamupemphera chikhululuko namutengera iye ku ntendere.’

(Al-Mu’jam-ul-Kabīr, vol. 10, pp. 198, Ḥadīṣ 10450; Tārīkh Dimashq, vol. 41, pp. 3)

Ilāhī khūb day day shauq Quran kī tilāwat kā

Sharaf day Gumbad-e-Khazrā kay sāye mayn shahādāt kā

*Pa chifukwa cha chikondi chofuna kuwerenga Quran,
ndikupempha kwa inu E Allah, mudzawutenge nzimu wanga
ngati wa yemwe wafera kunkhondo pansi pa denga la Mzikiti
wa Allah, lipangeni ili kukhala khumbo langa*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kupambana kophunzitsa vesi imodzi kapena Sunnah

Zafotokozedwa ndi Sayyidunā Anas رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ kuti waphunzitsa vesi imodzi ya Quran Yolemekezeka kapena Sunnah iliyonse ya Dīn kwa aliyense, Allah عَزَّوَجَلَّ adzamukonzera mphoto yake iyeyo pa Tsiku Lachiweruzo, imene siyidzapezekanso mphoto yabwino kwa aliyense yopambana kapena yoposera yake. (*Jam'ul-Jawāmi'*, vol. 7, pp. 281, Ḥadīṣ 22454)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Mphoto yabwino mpakana Tsiku Lachiweruzo kwa yemwe waphunzitsa vesi imodzi!

Zinafotokozedwa ndi mwini kupeza Nūr ziwiri, yemwenso ndi mtsonkhanitsi wa buku Lolemekezeka la Quran, Sayyidunā 'Uṣmān Ibn 'Affān رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ walankhula kuti, 'Munthu yemwe waphunzitsa vesi imodzi ya

Quran Yolemekezeka azalandira malipiro ochuluka kawiri poyerekeza ndi yemwe wayiphunzira [vesi imeneyo].’

Mu Ḥadīṣ ina, zafotokozedwa ndi Sayyidunā Anas رضى الله عنه Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ananena kuti, ‘Munthu yemwe angaphunzitse vesi imodzi ya Quran Yolemekezeka, kufikira ngati akupitiriza kuwerenga vesiyoyi, azakhala akulandira mphoto yabwino.’ (*Jam’-ul-Jawāmi’, vol. 7, pp. 282, Ḥadīṣ 22455-22456*)

Tilāwat kā jazbah ‘aṭā ker Ilāhī

Mu ‘āf farmā mayrī ḥar khaṭā Ilāhī

E Allah! Ndipaseni ine Chikondi chowerenga Quran – Ndipo ndikhululukireni machimo anga chifukwa cha chisoni chosatha

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Allah amawonjezera mphoto zochuluka kufikira Tsiku Lachiweruzo

Zafotokozedwa mu Ḥadīṣ, ‘Yense amene angaphunzitse vesi imodzi ya buku la Allah عَزَّوَجَلَّ kapena vesi imodzi ya maphunziro, Allah عَزَّوَجَلَّ azakhala akuchulikitsa mphoto yake ya zabwino kufikira Tsiku Lachiweluzo.’ (*Tārīkh Dimashq, vol. 59, pp. 290*)

‘Aṭā ḥo shauq Maulā Madrasay mayn ānay jānay kā

Khudāyā zauq day Quran paṛhnay kā paṛhānay kā

*E Mbuye Wanga! Ndipangeni ine kukhala wokonda kusaka
maphunziro a Chisilamu*

*O Allah! Ndipatseni chidwi komanso tunthu mukuphunzira
komanso kuphunzitsa buku Lolemekezeka la Quran*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Analoweza magawo 15 a Quran adakali mu mimba molemekezeka mwa mayi ake

Funso lofunikira kwambiri, komanso yankho lake – lochokera mu kunyezimira kwa chikhulupiriro, layikidwanso kuchokera mu buku lotchedwa *Malfūzāt-e-A’lā Ḥaḍrat*:

Funso: Olemekezeka! Kodi pali mulingo woziwika woyikidwa ndi Shari’ah pa ‘Taqrīb-e-Bismillāh¹’?

Yankho: Palibe chomwe chayikidwa mulingo ndi Shari’ah [pa zinthu zonga zimenezi], komabe, pa zaka 4, miyezi 4 komanso masiku 4 analingaliridwa ndi kuyerekezedwa [pa chimenechi] ndi anthu ozama pa maphunziro achipembezo. Pamene Sayyidunā Shaykh Khuwājāh Quṭb-ul-Ḥaḡ Waddīn Bakhtiyār Kākī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anali wa zaka 4, miyezi 4 komanso masiku 4 akubadwa, dongotsolo lake lopanga ‘Taqrīb-e-Bismillāh’ linakhazikitsidwa ndipo anthu anayitanidwa. Sayyidunā Shaykh Khuwājāh Gharīb Nawāz رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anali

¹ Mwambo wophunzitsa kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran kwa mwana.

pomwepo ndipo anali ndi chitsimikizo kukuwuza mwanayo kuti awerenge بِسْمِ اللَّهِ, koma mosatenga nthawi anali mu Uzimu [Ilhām], ‘ndipo nthawi yomweyo anati, Ḥamīduddīn Nāgorī akubwera ndipo azaphunzitsa [mwanayu kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ].’ Ndipo ndi nthawi yomweyo ku Nāgor, Qāḍī Ḥamīduddīn رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ analandira uthenga wa Mulungu mu uzimu kuti anyamuke ndikupita kukamuphunzitsa m’modzi wa akapolo ake Allah kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ. Nthawi yomweyo, anafika pa malowa nati kwa mwanayo, ‘Mnyamata! Werenga بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ.’ Mnyamatatu anayamba kuwerenga ‘أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ’ ndipo anapitilira kuwerenga buku Lolemekezeka la Quraniyi kuyambira kumayambiriro kufikira anamaliza magawo 15 pa ntima osawonera.

Shaykh Qāḍī Ḥamīduddīn and Shaykh Khuwājāḥ Gharīb Nawāz رَحْمَةُ اللَّهِ anati kwa iye, ‘Mnyamata! Pitiriza kuwerenga!’ Iye anati poyankha, ‘Ndinanva ndikuloweza zochuluka chonchi ndikanali m’mimba molemekezeka mwa Mayi anga, ndipo ndi mulingo okhawu umene iwo anali ataloweza, ndipo inenso ndinali kuwerenga ndikuloweza magawo omwewo!’

(*Malfūzāt-e-A’lā Ḥaḍrat, pp. 481*)

Timpemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti awachitire chisoni iwo komanso atikhululukire ife ndi chisoni chake!

أَمِينَ بِجَاهِ النَّبِيِّ الْأَمِينِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Khudā Apnī ulfat mayn ṣādiq banā day

Mujhāy Mustafā kā Tū ‘āshiq banā day

*E Allah! Ndipangeni ine kukhala mu chikondi cheni cheni pa Inu
Ndipo ndipangeni ine kukhala wozipereka ndi tunthu
mukutsatira Mtumiki wanunso!*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Chonvetsa chisoni ndi chakuti, chifukwa cha kusowekera kwa Maphunziro Achisilamu, Asilamu ambiri lero sakudziwa malamuro Shari’ah okhuza kawerengedwe kolondora ka Quran, kuphunzitsa Quran, kunvesera Quran, kugwira Quran, ndi zina zotero. Ndi cholinga chofuna kuphunzitsa maphunziro a Chisilamu, komanso ndi chitsimikizo chofuna kuwapulumutsa Asilamu ochuluka ku uchimo osiyanasiyana, phata lodzadza ndi mitundu ya maluwa angale za Madani laperekedwa.

Ngale 21 za Madani zokhuza kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran

1. Amīr-ul-Mu`minīn, Sayyidunā ‘Umar Fārūq-e-A’zam رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ anali kuphyophyona buku Lolemekezeka la Quran mamawa wa tsiku lililonse, ndipo anali kunena, ‘Ichi ndi chipangano cha Mbuye wanga عَزَّوَجَلَّ, komanso ndi Buku

lake.’ (*Durr-e-Mukhtār, vol. 9, pp. 634*)

2. Ndi Mustahab kuwerenga Ta’awwuz ‘أَعُوْذُ بِاللّٰهِ’ pamene mukuyamba Tilawah, ndipo ndi Sunnah kuwerenga Tasmiyah ‘بِسْمِ اللّٰهِ’ kumayambiro kwa Sūrah, apo ayi ndiye kuti ndi Mustahab.

(*Bahār-e-Sharī’at, vol. 1, Gawo 3, pp. 550*)

3. Ngati Tilawah yayambira pa Sūrah At-Taubaḥ, ndiye kuti muzawerenga zonse Ta’awwuz komanso Tasmiyah; komano, ngati Tilawah yayambika kale musanafike malo amenewo, kenako Sūrah At-Taubaḥ ndikumabwera nkati kati mowerenga, ndiye kuti kuwerenga Tasmiyah sikuzafunikira. Mawerengedwe a Ta’awwuz munjira yosankhika kumayambiro kwa Sūrah imeneyi, amene anayambitsidwa ndi ena mwa ma Huffāz a mibado ino ndi wopanda chiyambi mu Chipembezo. Koposaposa, kufala kwa maganizo athu ambiri mwa ife pa kusapanga Tasmiyah ngakhale kumayambiro kwa Sūrah At-Taubaḥ kumeneko ndikosalondora. (*ibid, pp. 551*)
4. Ndi Mustahab kupanga Tilawah uli ndi Wuḍhū, molunjika ku Qiblah, komanso utavala zovala zabwino.

(*ibid, pp. 550*)

5. Kuwerenga Quran Yolemekezeka powonera ndi kwabwino kwambiri kuyerekeza ndi kuwerenga ya pantima, chifukwa mukuwonera munthu samakhala kuti akuwerenga Quran yokha, koma kuti amakhala akuwonanso buku Lolemekezeka la Quran ngakhaleenso kuligwira kumene, ndipo onsewa ndimachitidwe opembeza. *(Ghunya-tul-Mutamallī, pp. 495)*
6. Quran Yolemekezeka ikufunika iziwerengedwa ndi mawu abwino kwambiri, ndipo ngati wina alibe mawu abwino ndi opereka chikoka, akuyenera kukongoletsa mawu akewo. Komabe, sizololedwa kuwerenga ndi mawu amene angapangitse kusatchula bwino kwa mawu ndi zilembo, kuchotsera kapena kuwonjezera zilembo, ngati momwe oyimba amachitira. Munthu akuyenera kusamalitsa kwambiri mukusamala malamuro owerenga [Tajwīd].
(Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muhtār, vol. 9, pp. 694)
7. Ndizofunikira kwambiri kuwerenga Quran mokweza mawu, maka ngati palibe chiwopsezo chobweretsa chisokonezo kwa yemwe akupemphera, yense yemwe sakupeza bwino nthupi ngakhaleenso yemwe akugona.
(Ghunya-tul-Mutamallī, pp. 497)
8. Pamene vesi za Quran Yolemekezeka zikuwerengedwa mokweza mawu, anthu ena, ngakhale amakhala chete,

amapitiridza kuyang'ana kapena kuchita zinthu zosiyanasiyana. Anthu otelewa akuyenera kuzindikira kuti kunvetseranso ndikofunikira kwambiri pa mwamba pakukhala chete. Mu kulemekeza kumeneku, A'lā Ḥaḍrat, amene ndi mtsogoleri wa Aḥl-e-Sunnat, Shaykh Imām Aḥmad Razā Khān عَلِيٌّ مُحَمَّدٌ الرَّحْمَنُ afotokoza pa tsamba 352 la voluyome 23 ya *Fatāwā Razawīyyah*, 'Ndi Farḍ [zokakamizika] kunvetsera mwatchelu komanso kukhala chete pamene buku Lolemekezeka la Quran likuwerengedwa. Allah عَزَّوَجَلَّ walankhula kuti:

وَ إِذَا قُرِئَ الْقُرْآنُ فَاسْتَمِعُوا لَهُ وَأَنْصِتُوا لَعَلَّكُمْ تُرْحَمُونَ ﴿٢٠٣﴾

Ndipo Quran Yolemekezeka ikamawerengedwa, mvetselani mwatchelu ndikukhala chete, ndi cholinga choti muchitilidwe chisoni.'

[Kanz-ul-Īmān (Translation of Quran)] (Gawo 9, Al-A'rāf, verse 204)

9. Pamene Quran Yolemekezeka ikuwerengedwa mofuwula, ndi Zokakamizika kwa onse amene akupezeka pa malopo maka ngati onse asonkhana ndi cholinga chonvetsera kuwerengedwako. Apo ayi, kuzakhala kokwanira ngati m'modzi wa iwo akunvetsera, pamene ena akupitiriza kupanga zochitika zawo. (*Fatāwā Razawīyyah – umboni, vol. 23, pp. 353*)

10. Ndi Ḥarām kwa aliyense kuwerenga mokweza mawu pamene tili pa gulu. M'mikumano ya Īṣāl-e-Šawāb, nthawi zambiri anthu amasankha kuwerenga mokweza mawu – mchitidwe umenewu ndi Ḥarām [zolesedwelatu]. Ngati anthu ambiri akuwerengera malo amodzi, lamuro lawo iwowo lidzakhala loti akuyenera kuwerenga mwa chete.

(Bahār-e-Sharī'at, vol. 1, gawo 2, pp. 552)

11. Ngati, wina akuwerengera mu Masjid, m'mene ena akupemphera Ṣalāḥ kapena kuwerenga chilichonse cha Chipembedzo, ukuyenera kukweza mawu mu mulingo umene uziwunva wekha; mawuwa asamamupeze munthu wina wachifupi nawe.

12. Ndizosaloledwa kuwerenga mokweza mawu buku Lolemekezeka la Quran mu nsika, kapena paliponse pamene anthu akugwira ntchito.

(Ghunya-tul-Mutamallī, pp. 497)

13. Ndizoletsedwanso kuwerenga mokweza mawu pamene wina akuphunzira maphunziro a Chisilamu, kapena pamene wophunzira wa Chisilamu akubwereza kapena akufufuza maphunziro ake asayansi. *(ibid)*

14. Palibe kulakwika kulikonse pamene munthu akuwerenga Quran Yolemekezeka ali chigonere, koma ngati miyendo

yake ili chipindire [osayitambatsula] ndipo osaziphimba nkhope. Kuwonjezera apo, ndizolesedwa kupanga Tilāwah pamene mukuyenda kapena kugwira ntchito, maka ngati chidwi komanso kukhazikika kwa ntima sikunasokonezedwe; apo ayi kuwerenga kumeneko kuzakhala Makrūh [kodedwa]. (*ibid*, pp. 496)

15. Ndizosaloledwa kuwerenga Quran Yolemekezeka mu bafa kapena malo amene mumapezeka unwe uliwonse. (*ibid*)

16. Kunvetsera mwatchelu kuwerengedwa kwa Quran Yolemekezeka ndi kopambana kwambiri kuyerekeza ndi kuwerenga Quran Yolemekezekayi kapena kupemphera Nafl Ṣalāh [Mapemphero akufuna kwako].

(*ibid*, pp. 497)

17. Ngati wina wawerenga mosalondola, ndi Wājib yense akunvetsera kumukonza munthuyo, maka kumukonzako kukhale munjira yoti singabweretse udani kapena kaduka mwanjira iliyonse. (*ibid*, pp. 498)

18. Chimodzimodzi, ngati wina wabwereka buku Lolemekezeka la Quran, ndipo napeza vuto lililonse ngati mukalembedwe kapena katanthawuziridwe nkati mwake, ndi Wājib kwa iyeyo kumudziwitsa wina wake. (*Bahār-e-Sharī'at*, vol. 1, gawo 3, pp. 553)

19. Mu nyengo yosadzidzira, ndizopambana kwambiri kumaliza kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran ku m'mawa, pomwe nthawi yodzidzira, ndizopambana kwambiri kuwerenga buku Lolemekezeka la Quran gawo loyamba la Usiku, chifukwa umu ndi momwe Ḥadīṣ yanenera motere, 'Munthu yemwe wamaliza kuwerenga Quran Yolemekezeka kumayambiriro kwa tsiku, angelo azamupemphera chikhululuko iye kufikira dzuwa litalowa, ndipo yemwe angamalize gawo loyambirira la usiku, angelo adzamupemphera chikhululuko kufikira m'mawa.'

Ndipo chifukwa cha kutalika kwa usana mu nyengo ya chilimwe, kumaliza kuwerenga Quran Yolemekezeka mu nthawi yaku m'mawa kudzapangitsa kupempheredwa kwanu chikhululuko ndi angelo kwa nthawi yochuluka. Kulankhula kwina, usiku ndi wawutali mu nyengo ya chilimwe; zomwe zikutipasa kunvesetsa kuti kuwerenga Quran Yolemekezekayi mu gawo loyamba la usiku, kudzapangitsa kupempheredwa kwanu ndi angelo kuchulukenso [kupempheredwa] kwa chikhululuko.

(Ghunya-tul-Mutamalli, pp. 496)

20. Pamene Quran Yolemekezeka yonse yatha kuwerengedwa, ndizabwino kwambiri kuwerenga Sūraḥ Al-Ikhlāṣ katatu. Izi zidzakhalanso chimodzimodzi pomwe tikupemphera Tarāwīḥ Ṣalāḥ; komabe, ngati kumalizako kwachitika mu

Farḍ Ṣalāḥ, osazawerenga Sūraḥ Al-Ikhlāṣ kopitirira kamodzi. (*ibid*)

21. Pomaliza kuwerenga Quran Yolemekezeka, pambuyo pa Sūraḥ An-Nās, werengani Sūraḥ Al-Fātiḥah komanso Sūraḥ Al-Baqarah kufikira pa vesi iyi وَأُولَٰئِكَ هُمُ الْمُفْلِحُونَ ﴿١٠٢﴾, ndipo kenako pangani Du'a [pemphero], chifu kutero ndi Sunnah.

Mukulemekeza kumeneku, Sayyidunā ‘Abdullāḥ Bin ‘Abbās رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمَا akufotokoza kucho kwa Sayyidunā Ubayy Bin Ka'b رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ, ‘Pamene Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ anali kuwerenga ‘قُلْ أَعُوذُ بِرَبِّ النَّاسِ ﴿١﴾’, Iye anali kuyamba ndi Sūraḥ Al-Fātiḥah, kenako Sūraḥ Al-Baqarah kufikira pa vesi iyi وَ أُولَٰئِكَ هُمُ الْمُفْلِحُونَ ﴿١٠٢﴾, kenako anali kupanga Du'a [pemphero] pambuyo pa kumaliza kwake kuwerenga Quran yonse, ndipo anali kusiya pomwepo.’

(*Al-Itqān fī ‘Ulūm-il-Quran, vol. 1, pp. 158*)

Mwana wa Madanī anawulura chinsinsi!

Sayyidunā Abū ‘Abdullāḥ رَحِمَهُ اللَّهُ عَلَيْهِ akufotokoza kuti, ‘Sayyidunā Shaykh Abul Ḥasan Muhammad Bin Aslam Ṭūsī عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي anali kusamala kwambiri pobisa ntchito zake zabwino, kufikira mulingo woti tsiku lina analankhula, ‘Ndikanakhala ndi kuthekera, Ndikanatha kubisa ngakhale kwa Kirāman Kātibīn

(angelo awiri olemekezeka amene amalemba ntchito za munthu) mukupembeza Allah ﷻ! Mufotokoziyu akupitiriza, ‘Ndinali pafupi kwambiri ndi Shaykh kwa zaka zopitirira makumi awiri [20] koma sindinawawonepo tsiku lina lililonse, kupatula Lachisanu basi, anali kupemphera ma Rak’āt awo awiri a Nafl Ṣalāh. Shaykh رحمه الله عليه anali kutenga ntchiko chawo cha madzi nalowa nayo mu chipinda chawo chopatulika natseka chitseko chake kuchokera nkati mwa chipindachi. Sindimapeza mpata owona chimene iwo رحمه الله عليه anali kuchita nchipindamu, kufikira tsiku lina, pamene mwana wawo wa mwamuna anayamba kulira mofuwula. Pomwe mayi ake olemekezeka anali kuyesetsa kumutonθοza mwanayu, Ndinafunsa kuti, ‘Ndi chifukwa chani mwanayu akulira kwambiri?’ Mayi Wolemekezeka anati kwa ine, ‘Bambo ake mwanayu (Sayyidunā Shaykh Abul Ḥasan Ṭūsī رحمه الله عليه) amawerenga Quran Yolemekezeka mchipinda ichi [ndi mantha akumuwopa Allah ﷻ], ndipo mwanayu amayamba kulira mofuwula kwambiri akanva kulira kwa bambo akewo!’

Shaykh Abū ‘Abdullāh رحمه الله عليه akufotokoza, ‘Shaykh Sayyidunā Abul Ḥasan Ṭūsī رحمه الله عليه, pofuna kuziteteza yekha kuchokera ku kuziwonesera, anali kusamala kwambiri mukubisa ntchito zake zabwino kufikira mulingo woti anali kusambitsa ndikusuka nkhope mu chipinda chake chopatulika asanatuluke kunja, anali kusambitsa nkhope yake komanso kupaka kohl zikope za maso ake olemekezeka, ndi choti asazindikiridwe ngakhale ndi

munthu m'modzi yemwe kuti anali kulira powona nkhope kapena maso ake!

(Hilya-tul-Awliyā, vol. 9, pp. 254)

Timupemphe Allah عَزَّوَجَلَّ kuti amuchitire chisoni ndikutikhululukira ife tonse ndi chisoni chake!

أَمِينَ بِجَاهِ النَّبِيِّ الْأَمِينِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Mayrā ḥar ‘amal bas Tayray wāsiṭay ḥo

Ker ikhlāṣ aysā ‘aṭā Yā Ilāhī

*Ndikupempha kuti ntchito yanga ikhale yofuna
kukusangalatsani Inu basi*

*Ndipo ndipangeni ine kukhala wokhulupirika pa chimenechi–
Limeneli ndilo pempho langa!*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

سُبْحَانَ اللَّهِ عَزَّوَجَلَّ! Tikukamba mwanjira ina kuti, awa ndi anthu amene anali ndi chikhulupiriro komanso chikondi cheni cheni amene anali kubisa ntchito zawo zabwino; koma za chisoni, pomwe mbali inayi, pali ena amene amapanga mosemphanitsa, amene akusowekera chikhulupiriro chachikulu ngati ambiri mwa ife, amene timalengedza komanso kuwonetsera ntchito iliyonse yabwino tingagwire kapen kuchita. Choyambirira ndi

chakuti, sitimakwanitsa kugwira komanso kupanga ntchito zabwino ndipo ngati pang'ono pokha takwanitsa kutero, timapezeka kuti tikutero poyiwonetsera kwa anthu!

Nafs-e-badkār nay dil per yeh qiyāmat tawrī

‘Amal-e-nayk kiyā bhī to chupānay na diyā

*Ntima wanga wofuna kuwonetsera zabwino zanga, wakuza
kwambiri nkati mwa ntimawu
Ngati ndinagwirapo ntchito yabwino, Sindinakwanitse kuyibisa*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ndi Farḍ kwa Msilamu aliyense kuwerenga Quran Yolemekezeka molondora komanso kupewa kuwerenga molakwika

Mtsogoleri wa Aḥl-e-Sunnat, ‘Allāmah Maulānā Al-Ḥāj Al-Ḥāfiẓ Al-Qārī Ash-Shāḥ Imām Aḥmad Razā Khān عَلَيْهِ رَحْمَةُ الرَّحْمٰن wafotokoza motere, ‘Palibe chikayiko, kuphunzira Tajwīd imene ingamupangitse munthu kutchula bwino komanso molondora chilembo¹ chilichonse ndikuzipulumutsa yekha ku kulakwitsa mukawerengedwe ndi Farḍ-e-‘Ayin [zokakamizika kwa gulu

¹Izi zikutanthawuza kutchula zilembo zonse za Quran kuchokera pamalo awo enieni otulutsira mawu, malinga ndi malamulo a Tajwid.

akachita m'modzi zikhala ngati onse achita].’ (*Fatāwā Razawiyyah – yafotokozera, vol. 6, pp. 343*)

Kupambana kwa mwana wa Madanī yemwe akuwerenga Quran

Allah ﷺ amafuna kupereka chilango kwa anthu, koma Iye ﷺ amanva ana akuwerenga Quran Yolemekezeka, Ndipo Iye ﷺ amachibweza chilangocho. (*Sunan Dārimī, vol. 2, pp. 530, Ḥadīṣ 3345*)

Ĥo karam Allah! Ḥāfiẓ Madanī munno kay ṭufayl

Jagmagātay Gumbad-e-Khazrā kī kirno kay ṭufayl

*E Allah! Tidalitseni ife chifukwa cha ana amenewa,
amene aloweza Quran Yolemekezeka*

*Tinali ife chifukwa cha Mzikiti Wolemekezeka wa Mtumiki,
umene kuwala kwake kunafikira dziko lonse*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

اَللّٰهُمَّ لِلّٰهِ ﷺ! Kuchokera m'mikumano ya Dawat-e-Islami – Bungwe limene silandale koma limafalitsa uthenga wa Quran komanso Sunnah – Malo ambiri akhazikitsidwa mu mayiko ochuluka pa dziko lonse lapansi, ndipo amatchedwa kuti Madrasa-tul-Madīnah.

Pamene tikulemba bukuli, Mu Pakistan mokha, muli anyamata

ndi atsikana 50,000 amene akuphunzitsidwa kuwerenga komanso kuloweza buku Lolemekezeka la Quran mwa ulele mu Madāris amenewa. Kuwonjezera apo, maphunziro a akulu akulu amene akufunisitsa kuti aziwerenga bwino komanso molondola buku Lolemekezeka la Quran, pansi pa Madrasa-tul-Madīnaḥ (a akulu akulu) akhazikitsidwanso M’masājid komanso m’malo ena. maphunziro amenewa ndi a anthu omwe amakhalira kutanganika ndi ntchito komanso zinthu zina zambiri masana, amaphunzitsidwa kawerengedwe kabwino komanso kolondola ka Quran Yolemekezeka ndi kuphatikidzapo ma Du’ā [pempheo] komanso ma Sunnaḥ, nthawi zambiri pambuyo pa Ṣalāt-ul-‘Ishā kwa pafupifupi mphindi makumi anayi [40]. **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ**! Malo ngati omwewa, pogwiritsa ntchito dzina lomweli, akhazikitsidwanso ena achizimayi.

Ngale 14 za Madanī zokhu Sajdaḥ Tilāwat

1. Sajdaḥ Tilāwat imakhala Wājib pamene munthu wawerenga kapena kunva kuwerengedwa kwa Vesi ya Sajdaḥ [kugwesa nkhope pansi]. (*Al-Ĥidāyah, vol. 1, pp. 78*)
2. Kuwerengedwa kwa Kumasulira kwa Vesi ya Sajdaḥ mu chilankhulo cha Persian kapena chilankhulo cha ntundu wina uliwonse kumapangisanso Sajdaḥ kukhala Wājib pa owerenga komanso onvesera, ndipo zimenezi sizidzatengera kuti munthuyo amazindikira kuti imeneyi

ndi Vesi ya Sajdah kapena ayi. Komabe nkofunikira kwambiri kumudziwitsa munthuyo kuti kumeneko kunali Kumasulira kwa Vesi la Sajdah ngati sakudziwa. Ndipo ngati kunali kuwerengedwa kwa vesi ya Sajdah, ndiye kuti sizidzafunikiranso kumudziwinsa wonveserayu kapena wonvera kuti yawerengedwayo ndi vesi ya Sajdah.

(Fatāwā ‘Ālamgīrī, vol. 1, pp. 133)

3. Ndilamuro la kawerengedwe ka Quran Yolemekezeka kuti kuchuluka kwa mulingo wofuwulira powerenga ukhale wonveka kwa iye akuwerenga ngati palibe choletsa chilichonse pa mulingowu. *(Bahār-e-Sharī’at, vol. 1, gawo 4, pp. 728)*
4. Sizimafunikira kweni kweni kuti yemwe akunvetserayo achite kutsimikiza mu ntima zonvera kuwerengedwa kwa Vesi ayi; Sajdah imakhala Wājib ngakhale itanveka kuwerengedwa kwake popanda chitsimikizo cha iye. *(Al-Hidāyah, vol. 1, pp. 78)*
5. Ngati Vesiyi itawerengedwa mofuwula ndi mulingo umene ukunveka, koma chifukwa cha kupitiriridwa ndi phokotso ndipo iye sanakwanitse kunva vesi ya Sajdah ikuwerengedwa imakhalabe Wājib pa iye. Komabe, ngati milomo yake inasuntha pang’ono koma mawu sanatulutsidwe, Sajdah siyidzakhala Wājib. *(Fatāwā ‘Ālamgīrī, vol. 1, pp. 132)*

6. Sizimafunikira pokha pokha munthu awerenge vesi yonse kuti Sajdah ikhale Wājib pa iye. Pongotchula liwu limene lakamba nkhani ya Sajdah, motsatizana ndi liwu poyambilira kapena pamapeto pake, zimakhala zokwanira[kuti ikhale Wājib].

(Rad-dul-Muhtār, vol. 2, pp. 694)

7. **Njira ya Sajdah Tilawat:** Njira ya Sunnah yopangira Sajdah ili motere: Kuyimirira, uku mukunena mawu oti **اللَّهُ أَكْبَرُ** kenako pitani pa Sajdah nthawi yomweyo ndikunena **سُبْحَنَ رَبِّيَ الْأَعْلَى** kosachepera katatu. Ndipo kenako munene **اللَّهُ أَكْبَرُ**, imirirani. Kunena **اللَّهُ أَكْبَرُ** musanawerenge komanso mukamaliza vesi ya Sajdah ndi Sunnah. Kuyimirira musanapite pa Sajdah komanso mukamaliza kupanga Sajdah m'chitidwe uwiri onsewu ndi Mustahab. *(Durr-e-Mukhtār, vol. 2, pp. 699)*

8. Sizimafunikira mpaka kukweza manja pamene mukunena kuti **اللَّهُ أَكْبَرُ** pofuna kupanga Sajdah Tilawat, ndipo sizimafunikiranso kuwerenga Tashahhud (Attahiyyāt) kapena kupanga Salām.

(Tanvīr-ul-Abṣār, vol. 2, pp. 700)

9. Pamene mukuyika chitsimikizo cha Sajdah Tilawat, sizimafunikira kulunjika chitsimikizo chanu pa vesi yosankhika; chitsimikizo chosalunjika pa vesi iliyonse ya

Sajdah Tilawat ndichokwanira. (*Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muhtār, vol. 2, pp. 699*)

10. Ngati vesi ya Sajdah yawerengedwa kunja kwa Ṣalāh, sizimakhala Wājib kupanga Sajdah nthawi yomweyo. Koma kuti zimakhala zabwino kwambiri kupanga nthawi yomweyo. Ngati munthu ali ndi Wuḍhū maka maka, choncho kuchedwetsa kupanga ndi Makrūh Tanzīhī. (*Durr-e-Mukhtār, vol. 2, pp. 703*)
11. Ngati sizingatheke kupanga Sajdah pa nthawi imeneyo pa chifukwa chilichonse, zimakhala Mustahab kwa owerenga ndi onvetsera kuwerenga:

سَمِعْنَا وَأَطَعْنَا غُفْرَانَكَ رَبَّنَا وَإِلَيْكَ الْمَصِيرُ ﴿٢٨٥﴾

Tanvera ndipo titsatira, tikupempha chikhululuko kuchokera kwa Inu, E Inu Mbuye wathu, ndipo kwa Inu ndi komwe tizayenera kubwerera.

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira la Quran)] (Gawo 3, Al-Baqarah, vesi 285)

(Rad-dul-Muhtār, vol. 2, pp. 703)

12. Ngati, mu Majlis¹ (kusonkhana) kumodzi, vesi imodzi ya Sajdah ikubwerezedwa kapena ikunveredwa, ndi Sajdah

¹ Pofuna kuzindikiritsa mawu oti Majlis ndi zambiri zokhuza misonkhano, perekani kwa atsindikidzi a Maktaba-tul-Madīnah: *Bahār-e-Sharī'at*, volume 1, gawo 4, tsamba 736.

imodzi yokha imene izakhale Wājib, ngakhale itanveka kuchokera kwa anthu osiyana. Chimodzimodzi, ngati wina wawerenga vesi [ya Sajdah], ndipo wanva kuchokera kwa munthu wina kuwerengedwa kwa vesi yomweyo, Sajdah imodzi yokha ndi yomwe idzakhale Wājib pa iye. (*Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muhtār, vol. 2, pp. 712*)

13. Ndi Makrūh Tahrimī kusiya kapena kudumpha vesi ya Sajdah pamene mukuwerenga Sūrah yonse. Palibe vuto mukuwerenga vesi ya Sajdah yokha; komabe, ndi zopambana kwambiri kuwerenga motsatiza kapena kutsogoza vesi zina pamwamba pa vesiyo.

(*Durr-e-Mukhtār, vol. 2, pp. 717*)

Pofuna kukwaniritsa zokhumba

14. Potengera ndi ziphunzitso za Imam Ḥanafī pali ma vesi khumi ndi anayi [14] a Sajdah mu buku Lolemekezeka la Quran, ndipo ngati ma vesi onsewa [14] adzawerengedwa mu Majlis imodzi pa chifukwa chilichonse, kenako ndikupangidwa ma Sajdah ochuluka, Allah عَزَّوَجَلَّ azakwaniritsa cholinga chimenechi, ngakhale munthu atapanga Sajdah pambuyo pa vesi iliyonse kapena azapanga ma Sajdah onse 14 pambuyo pomaliza kuwerenga ma vesi onse 14.

(*Bahār-e-Sharī'at, vol. 1, gawo 4, pp. 738*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Mavesi 14 a Sajdah

1. إِنَّ الَّذِينَ عِنْدَ رَبِّكَ لَا يَسْتَكْبِرُونَ عَنْ عِبَادَتِهِ وَيُسَبِّحُونَهُ وَلَهُ
يَسْجُدُونَ ﴿٢٠٦﴾
(Gawo 9, Sūrah Al-A'rāf, vesi 206)
2. وَلِلَّهِ يَسْجُدُ مَنْ فِي السَّمَوَاتِ وَالْأَرْضِ طَوْعًا وَكَرْهًا وَظِلَلُهُم بِالْغُدُوِّ
الْأَصَالِ ﴿١٦﴾
(Gawo 13, Sūrah Ar-Ra'd, vesi 15)
3. وَلِلَّهِ يَسْجُدُ مَا فِي السَّمَوَاتِ وَمَا فِي الْأَرْضِ مِنْ دَابَّةٍ وَالْمَلَائِكَةُ وَهُمْ
لَا يَسْتَكْبِرُونَ ﴿٢٩﴾
(Gawo 14, Sūrah An-Naḥl, vesi 49)
4. قُلْ آمِنُوا بِهِ أَوْ لَا تُؤْمِنُوا إِنَّ الَّذِينَ أُوتُوا الْعِلْمَ مِنْ قَبْلِهِ إِذَا يُتْلَى عَلَيْهِمْ
يَخِرُّونَ لِلْأَذْقَانِ سُجَّدًا ﴿١٢٤﴾ وَيَقُولُونَ سُبْحَنَ رَبِّنَا إِنْ كَانَ وَعْدُ رَبِّنَا لَمَفْعُولًا ﴿١٢٥﴾
وَيَخِرُّونَ لِلْأَذْقَانِ يَبْكُونَ وَيَزِيدُهُمْ خُشُوعًا ﴿١٢٦﴾
(Gawo 15, Sūrah Banī Isrā'īl, vesi 107-109)
5. إِذَا تُلِيَ عَلَيْهِمْ آيَاتُ الرَّحْمَنِ خَرُّوا سُجَّدًا وَبُكِيًّا ﴿٥١﴾
(Gawo 16, Sūrah Maryam, vesi 58)

6. أَلَمْ تَرَ أَنَّ اللَّهَ يَسْجُدُ لَهُ مَنْ فِي السَّمَوَاتِ وَمَنْ فِي الْأَرْضِ وَالشَّمْسُ وَالْقَمَرُ
وَالنُّجُومُ وَالْجِبَالُ وَالشَّجَرُ وَالدَّوَابُّ وَكَثِيرٌ مِنَ النَّاسِ ۖ وَكَثِيرٌ حَقَّ عَلَيْهِ
الْعَذَابُ ۚ وَمَنْ يُهِنِ اللَّهُ فَمَا لَهُ مِنْ مُكْرِمٍ ۖ إِنَّ اللَّهَ يَفْعَلُ مَا يَشَاءُ ﴿١٨﴾

(Gawo 17, Sūrah Hajj, vesi 18)

7. وَإِذَا قِيلَ لَهُمُ اسْجُدُوا لِلرَّحْمَنِ قَالُوا وَمَا الرَّحْمَنُ أَنَسْجُدُ لِمَا تَأْمُرُنَا
وَزَادَهُمْ نُفُورًا ﴿٢٠﴾

(Gawo 19, Sūrah Al-Furqān, vesi 60)

8. أَلَا يَسْجُدُوا لِلَّهِ الَّذِي يُخْرِجُ الْخَبَاءَ فِي السَّمَوَاتِ وَالْأَرْضِ وَيَعْلَمُ مَا تُخْفُونَ
وَمَا تُعْلِنُونَ ﴿٢٥﴾ اللَّهُ لَا إِلَهَ إِلَّا هُوَ رَبُّ الْعَرْشِ الْعَظِيمِ ﴿٢٦﴾

(Gawo 19, Sūrah An-Naml, vesi 25-26)

9. إِنَّمَا يُؤْمِنُ بِآيَاتِنَا الَّذِينَ إِذَا ذُكِّرُوا بِهَا خَرُّوا سُجَّدًا وَسَبَّحُوا بِحَمْدِ رَبِّهِمْ
وَهُمْ لَا يَسْتَكْبِرُونَ ﴿١٥﴾

(Gawo 21, Sūrah As-Sajdah, vesi 15)

10. فَاسْتَغْفِرْ رَبَّهُ وَخَرَّ رَاكِعًا وَأَنَابَ ﴿٢٣﴾ فَغَفَرْنَا لَهُ ذَلِكَ ۖ وَإِنَّ
لَهُ عِندَنَا لَمَزْنَةً وَحُسْنَ مَآبٍ ﴿٢٤﴾

(Gawo 23, Sūrah Şād, vesi 24-25)

11. وَمِنْ آيَاتِهِ اللَّيْلُ وَالنَّهَارُ وَالشَّمْسُ وَالْقَمَرُ لَا تَسْجُدُوا لِلشَّمْسِ وَلَا لِلْقَمَرِ
وَاسْجُدُوا لِلَّهِ الَّذِي خَلَقَهُنَّ إِن كُنتُمْ إِيَّاهُ تَعْبُدُونَ ﴿٣٧﴾ فَإِنْ اسْتَكْبَرُوا
فَالَّذِينَ عِنْدَ رَبِّكَ يُسَبِّحُونَ لَهُ بِاللَّيْلِ وَالنَّهَارِ وَهُمْ لَا يَسْأَمُونَ ﴿٣٨﴾
(Gawo 24, Sūrah Ḥā-Mīm As-Sajdah, vesi 37-38)

12. فَاسْجُدُوا لِلَّهِ وَاعْبُدُوا ﴿٦٢﴾
(Gawo 27, Sūrah Najam, verse 62)
13. فَمَا لَهُمْ لَا يُؤْمِنُونَ ﴿٢٠﴾ وَإِذَا قُرِئَ عَلَيْهِمُ الْقُرْآنُ لَا يَسْجُدُونَ ﴿٢١﴾
(Gawo 30, Sūrah Al-Inshiqāq, vesi 20-21)
14. وَاسْجُدْ وَاقْتَرِبْ ﴿١٩﴾
(Gawo 30, Sūrah Al-‘Alaq, vesi 19)

Ngale 9 za Madanī zokhuza kugwira buku Lolemekezeka la Quran

1. Pamene munthu alibe Wuḍhū [sanaziyeretse ku lisilo laling’ono], ndi Farḍ kupanga Wuḍhū ndi cholinga choti agwire Quran Yolemekezeka. (Nūr-ul-Īqāḥ, pp. 18)
2. Pamene munthu alibe Wuḍhū, ndizololedwa kuti awerenge Quran Yolemekezeka mowonera koma posayigwira.
3. Sizololedwa kupanga Tayammum ndi cholinga chogwira Quran Yolemekezeka, kuti mupange Sajdah Tilāwat,

kapena kupanga Sajdah Shukr [kugwetsa nkhope pansi kothokoza], pamene nvula yafika. (*Bahār-e-Sharī'at*, vol. 1, gawo 2, pp. 352)

4. Ndi Ḥarām kwa munthu yemwe Ghusl [kusamba] kuli Fard, kugwira Quran Yolemekezeka. Izi ndikuphatikizapo matsamba osalembedwa kanthu, chikutiro, komanso kansalu kamene mumayika pa mwamba pa Quran Yolemekezeka. Chimodzimodzi, ndi Ḥarām kuwerenga Quran Yolemekezeka pa ntima kapena mu ubongo, kulemba vesi, kulemba Ta'wīz la vesi, kuligwira Tawiz, kapena kuvala ndikukolekera chinthu chimene chatenga kapena kulembedwa vesi ya mu Quran mwachitsanzo kukolekera pa khosi chinthu chimene chalembedwa mawu a Muqatta'at¹.

(*Bahār-e-Sharī'at*, vol. 1, gawo 2, pp. 326)

5. Ngati Quran Yolemekezekayi ili mu chikwama, ndizololedwa kugwira chikwamacho. Ndizololedwanso kunyamula pogwiritsa ntchito kansalu ka m'manja kapena kalikonse koyera kuchokera ku unwe uliwonse kamene sikangapereke kuthekera kogwira Quran Yolemekezekayi poyikhuza. Ndi Ḥarām kugwira kapena kunyamula buku Lolemekezeka la Quran pogwiritsa ntchito malaya kapena

¹ ق - طه - يس - كهيعص - الم ndi zina mwa izo. Zimachtchedwa zilembo za Muqatta'at.

gawo lililonse la chovala cha pathupi lanu; ngakhale mpango wanu utakhala wawutali ndipo mwawuyika mu khosi lanu ukuzendewera, simukuyenera kugwiritsa ntchito gawo lina la mpangowu kugwira Quran Yolemekezeka, chifukwa nchitidwe uliwonse watchulidwawu umatengedwa wofunika kusamala munthu momwe tingakhalienso wosamala pogwira chikutiro cha Quran Yolemekezeka popeza chikutirocho ndi gawo lakenso. (*Durr-e-Mukhtār, Rad-dul-Muhtār, vol. 1, pp. 348*)

6. Malamuro a kuwerenga komanso kugwira Quran Yolemekezeka idzagwiritsidwanso ntchito pa Kumasulira kwa Quran Yolemekezeka mu chilankhulo cha Chichichewa, Persian, kapena chilankhulo cha ntundu uliwonse. (*Bahār-e-Sharī'at, gawo 2, pp. 327*)
7. Ndizosaloledwa kwa munthu yemwe alibe Wuḍhū kapena kwa yemwe Ghushl [kusamba] kuli kokakamizika, kugwira vesi yolembedwa mu buku kapena tsamba lankhani. Chimodzimodzi, ndizosaloledwanso kugwira kumbuyo kwa tsamba limene lalembedwa vesizi poganiza kuti mbali yomwe mwagwirayo siyinalembbedwe kanthu.
8. Munthu yemwe alibe Wuḍhū kapena yemwe Ghushl ikukakamizika pa iye, sakuloledwa kugwira kapena kukhuza gawo lililonse pa tsamba limene vesi ngakhale imodzi yokha yalembedwapo, ndipo palibe china chilichonse, chomwe chalembedwa; izi ndikuphatikizapo

kukhuza kutsogolo, kumbuyo, kwa matsamba ake ndi zina zotero.

Kalām-e-Pāk kay Maulā mujhay ādāb sikhilā day

Mujhay Ka'bah dikhā day Gumbad-e-Khazrā bhī dikhilā day

*Yā Allah! Ndipangeni ine kukhala ndi ntima wophunzira miyambo
yophunzilira Quran Yolemekezeka, komanso mwayi
Ndiwonetseni Ka'bah; komanso Mzikiti wanu, wodalitsika kwambiri*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Pempho la Madanī kwa otsindikidza

9. Ndipempho lowona ntima la Madanī kwa onse otsindikiza mabuku a Chipembedzo komanso ma dayale amene amatulutsidwa sabata iliyonse kuti apewe kuchokera ku mchitidwe woyika vesi kapena Kumasulira kwake pa mwamba kapena kuseli kwa chikutiro cha mabuku, madayale, timabuku ting'ono ting'ono ndi zina. Popeza pa kunyamula kapena kukhuza ambiri mwa Asilamu amakodwa ndi nsampha umenewu mosadzindikira ndipo amagwira kapena kukhuza vesizi alibe Wuḍhū.

Ndikulemekeza komweku, 'Allāmah Maulānā Al-Hāj Al-Hāfiẓ Al-Qārī Ash-Shāh Imām Aḥmad Razā Khān عَلَيْهِ السَّلَامُ wafotokoza pa tsamba 393 la voluyome 23 ya *Fatāwā Razawīyyah*, 'Kuyika vesi za Quran pa chikutiro chimene

chakutira bandulo kapena paketi ya nyuzi peparu kapena timabuku ting'ono tingo'no, kapena pa zinthu zina ngati makadi kapena inivolopu, zimakolezela kusalemekeza ndipo zizatengera ku Ḥarām, chifukwa litha kugwiridwa ndi woperekera nyuzi peparayu kapena ena amene alibe Wuḍhū kapena akufunikira Ghushl kumene, kapena ndi Kuffār [anthu osakhulupirira] omwe nthawi zonse amakhala osayera [mwachitsanzo popanda Ghushl], ndipo kutero ndi Ḥarām. Allah عَزَّوَجَلَّ akulankhula:

لَا يَمْسُهُ إِلَّا الْمُطَهَّرُونَ

Palibe yemwe akuloledwa kugwira kupatula yemwe ali woyera (Ali ndi Wuḍhū).

[Kanz-ul-Īmān (Kumasulira la Quran)]

Pakuti izi zitha kuyikidwa pansi nthawi zina ndi cholinga choyika zisindikizo; pamene zithanso kuchotsedwa ndikutayidwa m'malo amene mumatayidwa zinyalala, ndipo mchitidwe umenewu umakolezeledwa potsatila khalidwe la otsindikiza ndi olemba.'

*Kodi chikhulupiro ndi chani? Ndinayifunsa nzeru zanga
Ndipo nzeru zanga zinandiyankha: Chikhulupiro chili
kwambiri pa Kulemekeza*

سُبْحَانَ اللَّهِ عَزَّوَجَلَّ! Ngati mwapeza vesi ya mu Quran Yolemekezeka yayikidwa pa buku lina lililonse, zikupemphedwa kuti, pambuyo pokhala ndi zitsimikidzo zabwino, mudzawonetsa kwa otsindikidza, kapena mudzawatumizira fotokope yake kuzera pa chibaluwa [kapena imelo]. Mukulemba kwanu kukhale uthenga uwu, ‘Pambuyo powona vesi ya mu Quran Yolemekezeka pa chikutiro cha buku lanu lakuti ndi lakuti, Timapempha kuti muzizitalikira zoyika vesizi kapena Kumasulira kwake pa chikutiro cha mabuku, ndicholinga chofuna kuthandizira Asilamu ochuluka kupewa uchimo wogwira bukuli opanda Wuḍhū.’ جَزَاكَ اللَّهُ خَيْرًا

Ngati wotsindikidza mabukuyo amakonda ndikunvera anthu ophunzira bwino malamuro a Chisilamu إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ, adzakunverani komanso kukupempherani zabwino, ndipo azapanga chitsimikizo cha mphanvu chokhala watchelu kuzakonza chimenechi potsindikidza mabuku ena.

Maḥfūz Khudā rakhnā sadā bay-adabaun say

Aur mujh say bhī sarzad na kabhī bay-adabī hō

*E Allah! Nditetezeni ine nthawi zonse kwa anthu amene
salemekeza*

*Ndipo inenso ndisazapange uchimo wosalemekeza mwanjira
iliyonse*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ngale 4 za Madanī zokhuza kumasulira Quran Yolemekezeka

1. Kumasulira kwa Quran Yolemekezeka silimayenera kuwerengedwa popanda kuwerenga Tafsīr [ndemanga yofotokozera]. Chotsatira pamenepa ndi chidule cha Fatwā yolembedwa ndi A'lā Ḥaḍrat Imām Aḥmad Razā Khān عليه رَحْمَةُ الرَّحْمٰن, 'Ndizosatheka kupindula komanso kunvesetsa Quran Yolemekezeka powerenga Kumasulira kwake basi popanda kufotokozera kwake. Pa chilungamo chake, mukuwerenga Kumasulira chabe muli kuyipa kochuluka poyerekeza ndi ubwino wake.

Ngati munafunikira kuwerenga Kumasulira kwake, mukuyenera kutero ndi upangiri wochokera kwa akatswiri, ophunzira kwambiri komanso omuwopa Mulungu achi Sunnī.'

(Fatāwā Razawīyyah – referenced, vol. 23, pp. 382)

2. Pofuna kunvesetsa bwino Quran Yolemekezeka, pezani buku lanu lomasuliridwa ndi A'lā Ḥaḍrat, Wotsitsimutsa ma Sunnaḥ, mulondoleri wa 'Tarīqah, m'phunzitsi wa Sharī'aḥ, 'Allāmaḥ Maulānā Al-Ḥāj Al-Ḥāfiẓ Al-Qārī Ash-Shāḥ Imām Aḥmad Razā Khān عليه رَحْمَةُ الرَّحْمٰن, limene limatchedwa 'Kanz-ul-Īmān [chuma cha chikhulupiriro]', lomwe latenganso ndemanga zake kuchokera mu buku lotchedwa 'Khazāin-

ul-‘Irfān’ lolembedwa ndi ‘Allāmah Maulānā Sayyid Na’imuddīn Murādābādī عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْوَاهِدِي.

3. Pogwiritsa ntchito Madanī In’ām¹ yowerenga vesi zitatu [3] za Quran Yolemekezeka (poyamba ndi Kumasulira kenako ndemanga zake) tsiku lina lililonse; إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ muzaona nokha midalitso yake.
4. Kutengera dongotsolo la Bungwe la Dawat-e-Islami, Mzikiti wina uliwonse umatengedwa kukhala ngati Żaylī Ḥalqaḥ (nthambi yaying’ono). Cholinga cha Żaylī Ḥalqaḥ ndikukhazikitsa Madanī Ḥalqaḥ (malo ophunzilira) tsiku

¹ M’chikhalidwe cha Madani cha Dawat-e-Islami, muli Madanī In’āmāt [mafunso azochitika za Madani] okwanira 72 a abale achisilamu ndipo okwanira 63 a alongo achisilamu, omwe akonzedwa munjira ya mafunso m’kabuku kofuna kuthandiza Asilamu kukhala ndi moyo wachipembedzo komanso wabwino.

Iwo omwe ali ndi mwayi amachita Fikr-e-Madīnah [kudzifufuza pa zomwe achita] tsiku lililonse kwinku akuchonga m’abokosi omwe aperekedwa pa mayankho, ndipo kenako amapereka kabukuko kwa woyimira (Żimmaḥdār) wa m’dera lawo wa Dawat-e-Islami nkati mwa masiku 10 oyambirira a mwezi uliwonse watsopano wa Chisilamu.

Kuti mudziwe njira yonse ya izi, pezani kabuku kotchedwa ‘Madanī In’āmāt’ kuchokera ku Maktaba-tul-Madīnah [nthambi yofalitsa mabuku ya Dawat-e-Islami]. Mabuku ambiri ofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madīnah akupezeka pa webusayiti ya Dawat-e-Islami: www.dawateislami.net kuti mudawunirode kwawulere.

1’Ilm-ul-Kalām ndi nthambi ya maphunziro a Chisilamu yomwe imafotokoza mozama za makhalidwe a Allah عَزَّوَجَلَّ.

lililonse pambuyo pa Ṣalāt-ul-Fajr kuwerenga/kunvetsera vesi zitatu [3] za Quran Yolemekezeka ndi Kumasulira kwake kuchokera mu *Kanz-ul-Īmān* komanso ndemanga zake kuchokera mu *Khazāin-ul-ʿIrfān/Nūr-ul-ʿIrfān*. Ngati nkotheke, abambo onse akuyenera kuyesetsa kupeza m'dalitso umenewu ndikutenga nawo gawo mu Madanī Ḥalqaḥ amenewa.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ngale ziwiri za Madanī zokhuza

kakwiriridwe/kamizidwe ka matsamba othothoka a mu Quran Yolemekezeka

1. Ngati tsamba la mu Quran Yolemekezeka lafika posintha mawonekedwe ndikusawoneka bwino malemba chifukwa cha kukhalitsa ndipo pali kuthekera kwa kuwonongeka kwa matsambawo, akuyenera kukutiridwa mu kansalu koyera bwino ndikukwiriridwa pa malo otetezeka. Pamene matsambawa akukwiriridwa, Laḥad (ngati komwe amayikidwa msilamu pamene akuyidwa m'manda) lizayenera kukumbidwa (pambuyo pokumba dzenjelo, muzagoba mpata moyang'ana ku Qiblaḥ, mpata wawukulu ndithu wokwanira kuyika matsamba onse) ndi cholinga choti umve kapena zoyipa zilizonse zisagwerepo. Mwachidziwikire, kuyika matsamba malo otelewa,

kumakhala kuyika chitetezo, ndicholinga chofuna kutetezera matsambawa ku nyasi komanso unwe uliwonse. Ngati matsamba a buku Lolemekezeka la Quran akhalitsa, sakuyenera kuwotchedwa.

(Bahār-e-Sharī'at, gawo 16, pp. 138)

2. Matsamba opatulika a mu Quran Yolemekezeka sakuyenera kuponyedwa kapena kuyikidwa malo omwe si akuya mu nyanja, kapena omwe si akuya mu nsinje ngakhaleenso chitsime, chifukwa nthawi zambiri amayandama pamwamba kenako ndikutengedwa ndi madzi kupezeka m'mbali mwake ndipo zimabweletsa kusalemekeza kwakukulu. Njira yoyikira matsamba amenewa mu nyanja ndi imeneyi, kuyamba ndi kuwayika matsambawo mu thumba kapena chikwama, ndikumangirira mwala wolemera kwambiri ndikuyika mabowo pa thumba kapena pa chikwama kuti madzi alowe nthawi yomweyo ndikukwanitsa kumiza kufikira pansi. Ngati madzi sakulowa nkati mwake, Thumba kapena chikwamacho chitha kusinthidwa kwa malipande ndi ntunda wawutali kwambiri ndikutsakama pa ntunda.

Mukuzikonda kosayika mu thumba kapena chikwama, nthawi yakale, ngakhale nthawi yama Kuffār anali kupanga njira yomweyi ndipo kusambanga njira imeneyi kunali kutengedwa kusalemekeza kumene munthu aliynse wokhulupirira mowona ntima amakhala ndi mantha

komanso kunjenjemera akudziwa nkhani yotereyi. Ngati njira imodzi yofuna kutsimikidzira kuti Thumba kapena chikwama chafika ndikukhazikika pansi pa nyanjayo, Msilamu m'modzi wodziwa kusambira ndikumira atha kuthandidzira kukawona, komabe osayiwa kuti thumba kapena chikwama chomwe chayikidwa matsambawa chiyikidwe mibowo ing'ono ing'ono kuti madzi azilowa pofuna kutetezera ku chilichonse.

Mayn adab Quran kā hār ḥāl mayn kartā rahūn

Ḥār ghāṛī ay mayray Maulā Tujh say mayn dartā rahūn

*Ndikupemphera kuti ndikhale munthu wolemekeza Quran
nthawi zonse*

*E Allah! Chifukwa chokuwopani Inu nokha ndipangeni kuti
ndizinjenjemera nthawi zonse*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ngale 8 Zosiyanasiyana za Madani

1. Ndichikhalidwe chabwino kusunga Quran Yolemekezeka mu chikwama kapena malo amene pali chovindikira. Asilamu ochuluka akhala akupanga zimenezi kuyambira nthawi ya Masaḥābaḥ ndi Tābi'in رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُمْ أَجْمَعِينَ.

(Bahār-e-Sharī'at, gawo 12, pp. 139)

2. Limodzi mwa khalidwe lolemekezera Quran Yolemekezeka ndikupewa kuyitembenukira moyiwonetsa nsana, kutambatsula miyendo poyang'aniza kumbali yake, kunyamula mapazi kapena miyendo m'mwamba poyipitirira muyeso wake, kukhala malo okwera kwambiri poyerekedza ndi malo amene yayikidwa. (*ibid*)
3. Sayansi za Lughāt [zilankhulo] zitatu (3), Naḥw [malamuro achilankhulo: kalembedwe ka Arabic], ndi Şarf [phunziro lofufuza zambiri za zilembo] ndizofanana. Munthu akuloledwa kuyika buku lililonse pa mwamba pa lina. Ndipo pa mwamba pa mabukuwa, mabuku a 'Ilm-ul-Kalām¹ atha kuyikidwa; kenako pa mwamba pa mabuku amenewa, mabuku a Fiqh [phunziro la malamuro a Chisilamu] atha kuyikidwa; ndipo pa mwamba pake pa ma buku a Ḥadīṣ ndi Maduwa amene atchulidwa mu Quran komanso Ḥadīṣ atha kuyikidwa.

Kenako pa mwamba pa mabukuwa, ma buku a Tafsīr atha kuyikidwa; ndipo komalizira, pa mwamba pa mabuku onsewa, Quran Yolemekezeka idzayikidwe pa mwamba pake. Osayika chovala kapena chilichonse pa mwamba pa chikwama chimene mwayika Quran Yolemekezeka. (*Fatāwā*

‘Ālamgīrī, vol. 5, pp. 323-324)

¹ 'Ilm-ul-Kalām ndi nthambi ya maphunziro a Chisilamu yomwe imafotokoza mozama za makhalidwe a Allah عزوجل

4. Ngati wina akusunga Quran Yolemekezeka mnyumba mwake ndi chitsimikizo chopeza madalitso komanso zabwino, koma ndikusamayiwereka, sazapeza Machimo ayi. Maka pa chifukwa, cha chitsimikizo chakechi idzakhala njira imene azipezera mphoto yabwino. (*Fatāwā Qādī Khān, vol. 2, pp. 378*)
5. Ngati Quran Yolemekezeka yagwera pansi mwangozi kuchoka m’manja mwa wina kapena kukhwekhweredzeka, sikudzalembedwa tchimo lililonse ngakhale kupereka Kaffārah [chindapusa] chilichonse.
6. Ngati munthu wina **مَعَادَ اللَّهِ عَزَّوَجَلَّ** waponya pansi Quran Yolemekezeka ndi chitsimikizo chosayilemekeza, kapena kuyika mapazi ake pa mwamba pa Quran pofuna kuonetsa kusayilemekeza; amakhala Kāfir nthawi yomweyo.
7. Mawu amene alankhulidwa munjira yolumbirira (Qasam) kapena kulumbirira pogwira Quran Yolemekezeka m’manja kapena poyika dzanja lanu pa buku la Quran Yolemekezeka, kulumbirira kotereku kumatengedwa kowona ntima ndipo kowopsa kwambiri (Qasam). Komano, ngati walankhula mawu posatchula liwu lililonse logwilitsidwa ntchito polumbira m’manja mwake muli Quran kapena kuyika dzanja lake pa mwamba pa Quran Yolemekezeka, kulumbirako (Qasam) sikudzakhazikitsidwa ndipo munthuyo sadzapereka

Kaffārah [chindapusa] chilichonse. (*Fatāwā Razawīyyah* – vol. 13, pp. 574-575)

8. Ngakhale zitakhala kuti muli ndi ma Quran ochuluka mu Masjid (Mzikiti), koma mukugwiritsa ntchito ochepa chabe; ndipo ena akungokhala; ndizosaloledwa ngakhale pang’ono kugulitsa ngakhale mutayika chitsimikizo chogwiritsira ntchito ndalama yakeyo pa ntchito za Mzikiti. M’malo mwake, ma Quran amenewo atha kugawidwa m’malo ngati m’mala Masājid ndi m’mala Madāris.

(*Fatāwā Razawīyyah* – yafotokozero, vol. 16, pp. 164)

Ĥar roz mayn Quran paṛḥūn kāsh Khudāyā

Allah! Tilāwat mayn mayray dil ko lagā day

*E Mbuye wathu Allah! Kupangeni kuwerenga Quran
kukhala machitidwe anga a tsiku ndi tsiku!*

*Mukuwerenga Quran mwanga ndi ntima wonse,
ndipangeni ine kukhala keen!*

Ngale 5 za Madanī zokhuza kupanga Īṣāl-e-Ṣawāb

1. Mtumiki Wodalitsika komanso Wolemekezeka ﷺ walankhula kuti, ‘Nyengo ya munthu yemwe ali m’manda mwake imakhala ngati ya yemwe akumira m’madzi; amadikira ndikuyembekezera pemphero kuchokera kwa bambo ake, mayi ake, mchimwene wake kapena nzake. Pamene pemphero la wina aliyense wamumphera

zabwino limamupeza, amachitenga chimenechi ngati chothokozeka kwambiri kuposa chilichonse pa dziko la pansi ndi zonse zopezeka nkati mwake. Allah ﷻ amapereka Šawāb zomwe zaperekedwa ngati mphatso kuchokera kwa achibale ake monga mapirire. Ndipo pemphero la munthu yemwe ali moyo kumupemphera yemwe anamwalira ndikumupemphera chikhululuko.’

(Shu’ab-ul-Īmān, vol. 6, pp. 203, Ḥadīṣ 7905)

2. Zinasimbidwa mu buku lotchedwa *Ṭabarānī*, ‘Pamene munthu wina anatumiza Šawāb [mphoto yabwino] za ntchito zake zabwino kwa munthu womwalira, Jibrīl عليه السلام amayika Šawāb mu malo otetezeka komanso ozizirira bwino kenako ndikuyima pafupi ndi manda ndipo anati, ‘E inu anthu amene mumakhala m’manda! Abale anu atumiza zabwino; zilandireni.’ Pakunva za ichi, amasangalala kwambiri, pamene onse oyandikana nawo (omwalira omwe ayandikana nawo manda) ali kukukuta mano ndikusawusidwa.’ *(Al-Mu’jam-ul-Awsaṭ, vol. 5, pp. 37,*

Ḥadīṣ 6504)

Qabr mayn āh! Ghup andḥayrā ḥay

Fazl say karday chāndnā Yā Rab

Kalanga ine! Palibe chinthu chimene chili chowopsa kwambiri ngati mdima woyambirira kudzawupeza tsiku loyamba kupezeka m’manda

E Allah! Ndi chisoni chanu, zatiwalitsireni ndi kuwala kwanu

3. Kuwonjezera pa Īsāl-e-Šawāb yowerenga Quran Yolemekezeka, munthu atha kumapanga Īsāl-e-Šawāb pochita china chilichonse chabwino ngati chimene chili cha Farḍ, Wājib, Sunnaḥ, Nafl, Šalāḥ, kusala kudya, Zakāḥ, Hajj, kulalikirira kapena kupereka Dars, kuyenda limodzi mu Madanī Qāfilāḥ, kugwiritsa ntchito Madanī In'āmāt, kutenga nawo gawo mukuwayitanira anthu ku zabwino, kuwerenga buku la chipembedzo kapena kugwira ntchito mwakufuna kwanu maka mu zichitochito za Madanī.

Ndondomeko ya kapangidwe ka Īsāl-e-Šawāb

4. Īsāl-e-Šawāb sintchito yovuta kupanga ayi; Ndizokwaniranso kwa munthu kulankhula kapena kutsimikiza mu ntima kuti, 'E Allah عَزَّوَجَلَّ! Perekani zabwino za Quran Yolemekezeka ndawerengayi (kapena zabwino zimene wawerenga wakuti wakuti wanga) kwa malemu Mayi anga olemekezeka'. لَنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ ndipo Šawāb zikafikitsidwa.

Ndondomeko ya Fātiḥah

5. Fātiḥah komanso ndondomeko yake imene imapangidwa pakati pa Asilamu ochuluka masiku ano, maka pa chakudya, ndiyabwino kwambiri. Chifukwa imati ikatha ndondomekoyi, Īsāl-e-Šawāb ya kuwerenga Quran Yolemekezeka. Itha kutsatizira pambuyo pake. Yikani

chakudya chonse chikuphezeka pamene mukupanga Īṣāl-e-Šawāb patsogolo pake (kapena yikani chochepa chabe kuchokera mu ntundu uliwonse wa chakudya chomwe chakonzedwa), pamodzi ndi chikho cha madzi. Kenako werengani **أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ**, werengani Sūrah Al-Kāfirūn kamodzi:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

قُلْ يَا أَيُّهَا الْكَافِرُونَ ﴿١﴾ لَا أَعْبُدُ مَا تَعْبُدُونَ ﴿٢﴾ وَلَا أَنْتُمْ عِبُدُونَ مَا
أَعْبُدُ ﴿٣﴾ وَلَا أَنَا عَابِدٌ مَّا عَبَدْتُمْ ﴿٤﴾ وَلَا أَنْتُمْ عِبُدُونَ مَا أَعْبُدُ ﴿٥﴾
لَكُمْ دِينُكُمْ وَلِيَ دِينِ ﴿٦﴾

Werengani Sūrah Al-Ikhlās katatu (3):

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

قُلْ هُوَ اللَّهُ أَحَدٌ ﴿١﴾ اللَّهُ الصَّمَدُ ﴿٢﴾ لَمْ يَلِدْ ۖ وَلَمْ يُولَدْ ﴿٣﴾
وَلَمْ يَكُنْ لَهُ كُفُوًا أَحَدٌ ﴿٤﴾

Werengani Sūrah Al-Falaq kamodzi:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

قُلْ أَعُوذُ بِرَبِّ الْفَلَقِ ﴿١﴾ مِنْ شَرِّ مَا خَلَقَ ﴿٢﴾ وَمِنْ شَرِّ غَاسِقٍ إِذَا وَقَبَ ﴿٣﴾
وَمِنْ شَرِّ النَّفَّاثَاتِ فِي الْعُقَدِ ﴿٤﴾ وَمِنْ شَرِّ حَاسِدٍ إِذَا حَسَدَ ﴿٥﴾

Werengani Sūrah An-Nās kamodzi:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

قُلْ أَعُوذُ بِرَبِّ النَّاسِ ﴿١﴾ مَلِكِ النَّاسِ ﴿٢﴾ إِلَهِ النَّاسِ ﴿٣﴾ مِنْ شَرِّ
الْوَسْوَاسِ الْخَنَّاسِ ﴿٤﴾ الَّذِي يُوَسْوِسُ فِي صُدُورِ النَّاسِ ﴿٥﴾ مِنَ الْجِنَّةِ
وَالنَّاسِ ﴿٦﴾

Werengani Sūrah Al-Fātiḥah kamodzi:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ ﴿١﴾ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ﴿٢﴾ مَلِكِ يَوْمِ الدِّينِ ﴿٣﴾
إِيَّاكَ نَعْبُدُ وَإِيَّاكَ نَسْتَعِينُ ﴿٤﴾ اهْدِنَا الصِّرَاطَ الْمُسْتَقِيمَ ﴿٥﴾ صِرَاطَ
الَّذِينَ أَنْعَمْتَ عَلَيْهِمْ ۖ غَيْرِ الْمَغْضُوبِ عَلَيْهِمْ وَلَا الضَّالِّينَ ﴿٦﴾

Werengani vesi ili m'musiya kamodzi:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

الْمَ ۝ ذَٰلِكَ أَنْكِتُ لَا رَيْبَ ۝ فِيهِ ۝ هُدًى لِّلْمُتَّقِينَ ۝ الَّذِينَ
يُؤْمِنُونَ بِالْغَيْبِ وَيُقِيمُونَ الصَّلَاةَ وَمِمَّا رَزَقْنَاهُمْ يُنفِقُونَ ۝ وَالَّذِينَ
يُؤْمِنُونَ بِمَا أُنْزِلَ إِلَيْكَ وَمَا أُنْزِلَ مِن قَبْلِكَ ۖ وَبِالْآخِرَةِ هُمْ يُوقِنُونَ
۝ أُولَٰئِكَ عَلَىٰ هُدًى مِّن رَّبِّهِمْ ۖ وَأُولَٰئِكَ هُمُ الْمُفْلِحُونَ ۝

Kenako werengani mavesi asanu ali m'musiwa:

1. وَالْهُكْمُ إِلَهُ وَاحِدٌ ۖ لَا إِلَهَ إِلَّا هُوَ الرَّحْمَنُ الرَّحِيمُ ۝
(Gawo 2, Sūrah Al-Baqarah, vesi 163)
2. إِنَّ رَحْمَتَ اللَّهِ قَرِيبٌ مِّنَ الْمُحْسِنِينَ ۝
(Gawo 8, Sūrah Al-A'rāf, vesi 56)
3. وَمَا أَرْسَلْنَاكَ إِلَّا رَحْمَةً لِّلْعَالَمِينَ ۝
(Gawo 17, Sūrah Al-Anbiyā, vesi 107)

4. مَا كَانَ مُحَمَّدٌ أَبَا أَحَدٍ مِّن رِّجَالِكُمْ وَلَكِن رَّسُولَ اللَّهِ وَخَاتَمَ
النَّبِيِّينَ ۖ وَكَانَ اللَّهُ بِكُلِّ شَيْءٍ عَلِيمًا ﴿٤٠﴾

(Gawo 22, Sūrah Al-Aḥzāb, vesi 40)

5. إِنَّ اللَّهَ وَمَلَائِكَتَهُ يُصَلُّونَ عَلَى النَّبِيِّ ۚ يَا أَيُّهَا الَّذِينَ آمَنُوا
صَلُّوا عَلَيْهِ وَسَلِّمُوا تَسْلِيمًا ﴿٥٦﴾

(Gawo 22, Sūrah Al-Aḥzāb, vesi 56)

Tsopano nfunireni zabwino Mtumiki (Ṣalāt-‘Alan-Nabī):

صَلَّى اللَّهُ عَلَى النَّبِيِّ الْأُمِّيِّ وَآلِهِ
صَلَّى اللَّهُ تَعَالَى عَلَيْهِ وَسَلَّم ۖ صَلَوةٌ وَسَلَامٌ عَلَیْكَ يَا رَسُولَ اللَّهِ

Pambuyo pake, werengani vesi iyi:

سُبْحَنَ رَبِّكَ رَبِّ الْعِزَّةِ عَمَّا يَصِفُونَ ﴿١٨٠﴾
وَسَلَّمَ عَلَى الْمُرْسَلِينَ ﴿١٨١﴾ وَالْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ ﴿١٨٢﴾

(Gawo 23, Sūrah, Aṣ-Ṣāffāt, verse 180-182)

Kenako munthu yemwe akupanga Fātiḥah akuyenera kuwerenga mofuwula kuti ‘Al-Fātiḥah’. Ndipo onse amene

akupezeka pa malowa akuyenera kuwerenga Sūrah Al-Fātiḥah mositsa mawu, ndipo muwerengi yemwenso akutsogolera chilichonse pa malopa akuyenera kulengeza mopempha kuti, ‘Chonde ndipatseni Šawāb za kalikonse komwe mwawerenga’. Onse opezeka pa malowa akuyenera kunena, ‘Tapereka kwa Inu chilichonse’. Kenako yemwe amapanga Fātiḥah ndi yemwenso adzapange Īṣāl-e-Šawāb.

Ndondomeko ya kapangidwe ka Du’ā [pempho] la Īṣāl-e-Šawāb

E Allah عَزَّوَجَلَّ! Tipatseni ife Šawāb pa chilichonse chimene tawerenga pano (ngati chakudya ndi zina. zilipo, ndiye kuti muzayenera kutchulanso) ponena “Komanso ndi Šawāb za chakudya chomwe chakonzedwa malo ano ndi ntchito zina zonse zina zimene takwanitsa kupanga mu tsiku la lero, osati motengera kulondola kwa ntchito yomwe tagwirayo ayi, koma chifukwa cha Chisoni cha Inu chopanda malire; ndipo tumizandinso Šawāb zimenezi m’malo mwathu kwa Mtumiki Wolemekezeka komanso Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ. Ndipo kuzela kwa Iye Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, tumizani Šawāb zimenezi kwa atumiki onse عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ, kwa ophunzira onse odalitsika رَحِمَهُمُ اللهُ, ndi anthu onse ochita zabwino رَحِمَهُمُ اللهُ. Ndipo kuzela kwa Mtumiki wanu Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ tumizani Šawāb zimenezi kwa munthu wina aliyense komanso ziwanda kuyambira mu nthawi ya Sayyidunā Ādam عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ kufikira tsiku la

lero, ndi onse amene adzakhale akubadwa mtsogolo muno kufikira tsiku Lachiweruzo.

Pamene mukupanga izi, mutha kutchulanso mayina a anthu olungama amene mukufuna kuti Šawāb zotelezi zisawapitirire. Chimodzimodzi, perekani Šawāb kwa makolo anu olemekezeka, achibale komanso Murshid (wokuwongorerani mu uzimu). (Mayina amene amatchulidwa pamene mukupempha eni ake nawo amasangalala). Kenako mudzamalize pemphero lanu monga mwa nthawi zonse.

(Ngati china mwa chakudya cha mitundu yonse chinasonkhanitsidwa pamodzi ndi madzi ochepa chabe, ndiye kuti muchibwenzeretse ndi kuchiphatikidza chakudya chonse ndi madzi onse).

Šawāb a'māl kā Tū mayray puḥanchā sārī Ummat ko

Mujḥay bhī bakhsh Yā Rab bakhsh un kī piyārī Ummat ko

*Tumizani zabwino za ntchito zanga ku Ummaḥ onse
Ndikhululukireni komanso khululukirani Ummaḥ wonse wa
Wokondedwa wanu*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ngale 17 za Madanī zokhuza kumanga ‘Imāmah [Sunnah yomangira nduwira]

Poyambirira tinve kaye, ma Ḥadiṣ 6 olemekezeka

Mustafa ﷺ

1. Ma Rak’āt awiri (2) a Ṣalāh imene yapempheredwa mutamanga ‘Imāmah ndi abwino kwambiri kuposa kupemphera 70 Rak’āt musanavale ‘Imāmah.’ *(Al-Firdaus bimā Ṣaur-ul-Khaṭṭāb, vol. 2, pp. 265, Ḥadiṣ 3233)*
2. Kumanga ‘Imāmah pamwamba pa chisoti ndikusiya kwathu ndi ma Mushrikīn [opembeza mafano]. Chifukwa kupinda kulikonse kwa ‘Imāmah kumene munthu amakulunga mutu mozungulira mutu wake, adzapasidwa Nūr [kuwala] kumodzi Tsiku Lachiweluzo.’ *(Al-Jāmi’-uṣ-Ṣaghīr, pp. 353, Ḥadiṣ 5725)*
3. Palibe chikayiko, Allah عزوجل ndi Angelo ake olemekezeka amatumiza Ṣalāt pa Tsiku Lachisanu kwa yemwe amamanga ndikuvala ‘Imāmah.’
(Al-Firdaus bimā Ṣaur-ul-Khaṭṭāb, vol. 1, pp. 147, Ḥadiṣ 529)
4. Kupemphera Ṣalāh mutamanga ‘Imāmah kumafanana ndi kugwira ntchito zabwino kokwana ka 10,000.’ *(Al-Firdaus*

bimā Šaur-ul-Khaṭṭāb, vol. 2, pp. 406, Ḥadīṣ 3805; Fatāwā Razawīyyah – yafotokozera, vol. 6, pp. 220)

5. Ṣalāt-ul-Jumu'aḥ ipemphereni mutamanga 'Imāmaḥ chifukwa mphoto yake ndiyochuluka kusiyaana ka 70 mukapemphera wopanda kuyivala.

(Tārīkh Madīnah Dimashq li Ibn 'Asākir, vol. 37, pp. 355)

6. Ma 'Imāmaḥ ndi chipewa chachifumu cha Aluya, ndiye valani 'Imāmaḥ ndipo ulemelero wanu uzawonekera. Aliyense yemwe amavala 'Imāmaḥ; amapeza mphoto pa kupinda kulikonse [kwa 'Imāmaḥ imene iye akupinda mokulunga mutu wake].'

(Jam'-ul-Jawāmi', vol. 5, pp. 202, Ḥadīṣ 14536)

7. Zafotokozedwa pa tsamba 312 la buku la *Baḥār-e-Sharī'at*, lotsindikidzidwa ndi nthambi yotsindikidza ya Dawat-e-Islami, ya Maktaba-tul-Madīnaḥ, pa tsamba 303 la gawo 16, 'Mangani 'Imāmaḥ muli chiyimire, ndipo valani Pājāmaḥ [shalwār, nsalu yoziphimbira thupi lake lonse] mutakhala pansu. Yense yemwe angachite mosemphanisa zimenezi (mwachitsanzo amamanga 'Imāmaḥ ali chikhalire, komanso amavala nsalu yoziphimbira thupi lake lonse, ali chiyimire); azagwidwa ndi nthenda, imene izakhale yopanda mankhwala.'

8. Ndidzabwino kwambiri kupinda koyambirira kwa ‘Imāmaḥ kukhale kopita mbali ya kumanja kwa mutu.

(Fatāwā Razawiyyaḥ, vol. 22, pp. 199)

9. Shimlaḥ (mwachitsanzo gawo lomwe limazendewera ku nduwira) ya ‘Imāmaḥ ya Mtumiki Wodalitsika komanso Wokondedwa ﷺ inali nthawi zonse kuzendewera kumbuyo kwake kolemekezeka, nthawi zina inali kuzendewera mbali yake ya kumanja, ndipo nthawi zina anali kusiya ma Shimlaḥ awiri pakati pa mapewa ake awiri Wodalitsika. Kusiya Shimlaḥ mbali ya kumanzere ndikupanga mosemphana ndi Sunnaḥ. *(Ashi’a-tul-Lam’āt, vol. 3, pp. 582)*

10. Kutalika kwa Shimlaḥ ya ‘Imāmaḥ ikuyenera kukhala yosachepera kutalika kwa zala zinayi mulifupi, ndi mulingo wofika ku nsana, mwachitsanzo pafupi pafupi kutalika kwa nkono umodzi.

(Fatāwā Razawiyyaḥ, vol. 22, pp. 182)

11. Mangani ‘Imāmaḥ mutayima komanso moyang’ana ku Qiblaḥ. *(Kashf-ul-Iltibāṣ fīs-Tiḥbāb-il-Libāṣ lish-Shaykh ‘Abdul Ḥaq Dīhlvī, pp. 38)*

12. Sunnaḥ ya ‘Imāmaḥ isakhale yayifupi kupyola 2½ lifupi lake, ndipo isakhalenso kupyola malipande asanu ndi

limodzi (6), komanso (13) ikuyenereka kumangidwa monga m'mene imawonekera chimphika chobiriwira cha kumadina -mukamangidwe. (*Fatāwā Razawiyyah*, vol. 22, pp. 186)

14. Ngati muli ndi nsalu yayikulu imene mungakwanitse kupinda kangapo pomanga mutu wonse, izatengedwa kuti ndi 'Imāmaḥ. (15) Zimakhala Makrūḥ kumanga ndi nsalu yaying'ono imene itha kutha pomanga kamodzi kapena kawiri basi. (*Fatāwā Razawiyyah – yafotokozero*, vol. 7, pp. 299)

16. Ngati Imāmaḥ ikuvulidwa pa chifukwa choyenera ndipo pali chitsimikizo mu ntima choyibwenzeretsa, tchimo limodzi lizakhala likukhululukidwa pa kumasula kopindidwa kulikonse. (*Fatāwā Razawiyyah*, vol. 6, pp. 214)

17. 'Allāmaḥ Shaykh 'Abdul Ḥaq Muḥaddiṣ Dihlvi عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي anati, 'Imāmaḥ yodalitsika ya Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ inali yoyera kawiri kawiri, nthawi zina anali kuvala yakuda komanso nthawi zina yobiriwira.'

(*Kashf-ul-Iltibās fis-Tiḥbāb-il-Libās*, pp. 38)

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ! Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ yemwe anatumizidwa kukhala chisoni ku zolengedwa zonse anayenera kuzikongoletsa mutu wake pomanga 'Imāmaḥ yobiriwira, ndipo [pa chifukwa chimenechi] Dawat-e-Islami inasankha ntundu umenewu wa 'Imāmaḥ ngati chizindikiro.

Ntundu wobiriwira wa ‘Imāmaḥ umatanthawuzanji! Kubiriwira kowala, komwe kumawonekera pamwamba pa malo odalitsika, amene ali ku Makkaḥ komanso Madīnaḥ, Mtumiki wathu Wokondedwa ndi Wolemekezeka ﷺ malo amene akupuma mphika wake ndiwobiriwira! Onse womukonda Mtumiki anayeneranso kuwala ‘Imāmaḥ yobiriwira ndi cholinga chosunga mitu yawo mu ntundu wobiriwira komanso wokongola. Tiyenera kuzindikira kuti, ntundu wobiriwirawu usakhale wopyola kupita kokuda choncho ayi; m’ malo mwake ukuyenera kukhala wokongora komanso kuwala omawonekera ngakhale mu m’dima wa usiku, kuwala kwa kubiriwira kwake ndi ntundu wokhawo umene umawonekera ndi m’dalitso wa kubiriwira kwa Mphika.

Naḥīn ḥay chānd sūraj kī Madīnay ko koī ḥājat

Wahān dīn rāt un kā sabz gumbad jagmagātā ḥay

*Madīnaḥ samafunikira kuwala kwa mwezi, dzuwa,
ngakhalenso magetsi*

*Imasala kale ndi kuwala kwa Emerald ya Mzikiti wake, usana
ndi usiku!*

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Patsani kabukhu aka kwa munthu wina mukamaliza kuwerenga.

Pezani madalitso pogawira mabuku osindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madīnah komanso timapepala tili ndi "ngale za Madani" pa nthawi ya ukwati, maliro, Ijtimā'at, 'Urs, mndandanda wa Milād ndi zina zotero. Pangani kukhala chizolowezi kusunga mabuku ena m'sitolo mwanu kuti muzipatsa makasitomala anu monga mphoto ndi cholinga chofuna kupeza madalitso. Tumizani kosachepera kabukhu kamodzi kolimbikitsa kutsata Sunnah kapena kapepala kali ndi "ngale za Madani" ku nyumba iliyonse ya anthu oyandikana nanu pogwiritsa ntchito ana kapena anyamata ogulitsa manyuzipepala, pofuna kuwonjezera khama lofalitsa uthenga wa zabwino komanso kupeza mphoto yayikulu.

Tchatì chomasulira

ء	A/a	ڑ	Ř/ř	ل	L/l
ا	A/a	ز	Z/z	م	M/m
ب	B/b	ژ	X/x	ن	N/n
پ	P/p	س	S/s	و	V/v,
ت	T/t	ش	Sh/sh		W/w
ٹ	Ṭ/ṭ	ص	Ṣ/ṣ	ه / ه / ة	Ĥ/ĥ
ث	Ṣ/ṣ	ض	Ḍ/ḍ	ی	Y/y
ج	J/j	ط	Ṭ/ṭ	ے	Y/y
چ	Ch	ظ	Ẓ/ẓ	َ	A/a
ح	Ḥ/h	ع	‘	ُ	U/u
خ	Kh/kh	غ	Gh/gh	ِ	I/i
د	D/d	ف	F/f	و مدہ	Ū/ū
ڈ	Ḍ/ḍ	ق	Q/q	ی مدہ	Ī/ī
ذ	Ẓ/ẓ	ک	K/k	امدہ	Ā/ā
ر	R/r	گ	G/g		

Kuphuka kwa Sunnah

Mwa chisomo cha Allah, maSunnah (njira zosafira za Mtumiki) amaphanzisiwa komanso kuphanziriwa mochaluka mu chikhaliwe cha 'Madani' cha Dawa-e-Islami, gulu lapadriko lonse komanso lonachita ndale lophanzitika Quran komanso Sunnah. Ndi pempho la Madani kuti mukhale usika wose mu 'Jima' (masochikano) wofimbikitsa Sunnah ya sabata iliyonse, yomwe imachitika pamubuyo pa 'Salat-ul-Maghrib' Lachinayi lililonse mu rutinda wawa, chifukwa chofera kusangalatsa Allah ndi zolinga sabwino. Ndi cholinga chofuna kupeta mphotho, chikhale chinoloweri chanu kuyenda mu 'Madani Qillah' (magulu oyenda) olimbikitsa Sunnah, ndi okonda Rasul (Mtumiki), kulumba nkabuka kuse ka 'Madani In'amaf' tika lililonse mukuchita 'Fikr-e-Madinah' (kuganizira za Madinah) ndikupereka kwa m'bile wa Chisilamu woyenera wa dera lano nkati mwa masiku khumi oyambirira a mwezi uliyonse wa Chisilamu. Kufirira mu madalitso a tili, modrakulitsa malingaliro ndi chilakolako chokhazikitsa MaSunnah, kulhala ndi chidazi cha machimo ndikutitiza chikhaliweiro chanu

Mhabe aliyenye wa Chisilamu ayenema kukulitisa malingaito a Madani akuti Ndiyenema kuyesetisa kudrikonisa ndekha ndi anhu a driko loise lapansi. [👉👉👉👉👉](#) Kuti bidrikonise toika, tiyenema kuchita malinga ndi Madani In'amut ndikuyesetisa kukonisa anhu a driko loise lapansi, tiyenema kuvenda ndi wa Madani Oqulab. [👉👉👉👉👉](#)



ISBN 978-089-631-228-6



0007-1226

Likulu la Madani Lapadziko Lense, Faizan-e-Madinah, Mahalliah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan.

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 1262

Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net